| | | | |
|---|---|---|---|
| **Mwayi** | luck, chance | **-lemera** | be rich; heavy |
| **Tsoka** | misfortune | **-sauka** | be poor; suffer |
| **Umphawi** | poverty | **-pepuka** | be light |
| **Usiwa** | shabbiness | **-zolowera** | get accustomed |
| **Nsanza** | rag | **-khoza** | succeed; do right |
| **Chuma** | wealth, riches | **-lakwa** | do wrong; be mistaken |
| **Mayeso** | trial, test, exam | **-fotokoza** | explain |
| **Khama** | stubborness perserverance | **-nyada** | be proud |

**AMENE** We come back to this Relative pronoun to see its application to the additional classes of nouns and to the propositions.

"who, which" (subject) : **Ana amene anakhoza mayeso ali ndi mwayi.** p. 14
"whom, which" (object) : **Anyamata amene munawaitana sanabwere.** p. 26
"whose" (possessive) : **Kaitaneni anthu amene ana ao sali pasukulu.** p. 39

It is sometimes dropped, more particularly with Demonstratives:
**Kodi buku mukuwerengali ndi la yani? — Mwini wake wasowa.**
**Kodi mukumbukira dzina lake la munthu uja tinakomana naye kumsika?**

D. Kamene **Mwaika kuti kansaru kaja (kamene) kanali patebulo apo?**
Timene **Timbalame timene tili pabwalo apo timadya chiyani?**
I. Kumene **Kodi mwakonza chakudya? — Ndili kuphika kumene** exactly.
Pamene where **Pamudzi pamene timakhala ife pali sitoro ziwiri.**
**Pamene mukufuna kumanga nyumba yanu ndi pati?**

when **Pameno ndinafika kwathu mfumu anandiitana.**
**Pamene munali kuulendo, mkazi wanu anamwalira.**

Kumene where **Kumudzi kumene mnzathu anakwatira ndi kwa yani?**
**Sindikudziwa kumene mng'ono wanga wapita.**
**Kumudzi kumene kwagwa maliro ndi kwa Chimutu.**

Mmene where **Tinagona mnyumba mmene munali katundu wambiri.**
**Umu ndi mmene timakonda kucheza kawirikawiri.**

when **Mmene tinali kudya nsima, mvula inayamba kugwa.**
**Simuyenera kuseka mmene anzanu ali kuimba nyimbo.**

how **Tiene mmene muphikira ndiwozo!** Note suffix **-ra** p. 81
**Mundiuze mmene mwachitira! Sindikudziwa mmene aliri.**

**Tsiku limene tinamanga ukwati wathu, kunali mvula yokhayokha.**
**Nthawi imene munanditana ine kunalibe; ndinali kudambo.**
**Nonsenu mwalakwa, tate wanu, mayi wanu, inu amene.** yourself.

**AMENEYU** This combination of **Amene** with **uyu or uyo** constitutes a second form of Demonstratives, with the same meaning "this" or "that". It suppoese that the object is being mentioned for the second time: "this" man about whom we are speaking...

| | | | |
|---|---|---|---|
| 1 | **Ameneyu** | **Amenewa** | **Kodi ali ndi akazi ena?** |
| 2 | **Umenewu** | **Imeneyi** | **— Inde ali nawo koma wamkulu ndi ameneyu.** |
| 3 | **Chimenechi** | **Zimenezi** | **Kumudzi kwathu kuli munthu wina dzina lake** |
| 4 | **Imeneyi** | **Zimenezi** | **Kalinda. Munthu ameneyo ali wamtali zedi.** |
| 5 | **Limeneli** | **Amenewa** | **Anafuna kuti msonkhano wao ukhale loweruka;** |
| 6 | **Umenewu** | **Amenewa** | **koma tsiku limenelo kunagwa mvula.** |
| D | **Kameneka** | **Timeneti** | **Kodi kamalaya kaja munagula dzulo ndi aka?** |
| I | **Kumeneku** | | **— Inde, ndi kameneka.** |

**Pamenepa** **Kodi pamene mukufuna kumanga nyumba yanu ndi apa? — Inde, ndi pamenepa.** here
**Kumeneku** **Tiyeni, tikakhale ku mpandaku!**
**— Iai; kumeneku kuli anthu.**
**Mmenemu** **Mnyumba umu simugona anthu masiku ano.**
**Ngati simupeza malo kwina, chabwino, mungathe kugona mmenemu.**

With **uyo** we have a similar construction: **Ameneyo Amenewo...**
**Kameneko Timeneto:** **Pamenepo, Kumeneko, Mmenemo** there

**-li ndi mwayi: -li mwayi: -chita mwayi** be lucky
**-chita khama** persevere, be stubborn. **Kanthu ndi khama!**
**-khoza** mayeso succeed a test. **Kulemba sindikhoza ( : sindidziwa)**
**-lakwa mayeso** fail: **-lephera mayeso: jomba. Cholakwa:** a mistake
**Munthu wolemera** rich. **Katundu wolemera** (different intonation) heavy
**Mmphawi:** munthu wosauka, wopanda ndalama.

1. Do you know the time when the accident happened?— It was at noon.
2. I cannot sleep in a house where there is much smoke.
3. There is a burial in the village where you are going.
4. I don't remember how my sister sings that song.
5. Five years ago he was very poor; but now he has become rich.
6. Persevere, don't lose heart; and you will succeed.
7. I hear that you lost your axe. Perhaps it is this one?
8. I don't know where the meeting will take place. Perhaps at Chimutu.
9. At the beginning I suffered much; but now I have got accustomed.
10. She is not lucky. She had three daughters and all of them died.

**Proverb: Tsoka sasimba koma mwayi.**